


KULIZINDIKIRA THUPI

LA AMBUYE

 Zikomo inu, M'bale Sullivan. Usiku wabwino, abwenzi. Ndi. . . Khalani pansi.

² Ndi chabwino kukhala tiri muno kachiwiri, usikuuno, pansi pa denga ili ndi pakati pa anthu abwino Achikhristu awa. Ndipo ife tikuyembekezera Mulungu, usikuuno, kuti achita mopitirira, mochuluka, pamwamba pa zonse zomwe ife tikanakhoza kuzichita kapena kuganiza. Ife tikudziwa kuti Iye ndi weniweni.

³ Ndi angati mukumverera kuti munachiritsidwa usiku watha, mu misonkhano? O, izo nzabwino basi. Ife tikuyembekezera kuti ena nonse inu kuti muchiritsidwe usikuuno. Ndipo i—ine ndikuganiza ife tatulutsabe makadi a pemphero. Billy sanapereke aliwonse, iye anandiuza ine, chifukwa kuti ife sitinatenge koma pang'ono okha aja a usiku watha. Ndipo pakhoza kukhala pali ena a anthu awo omwe anamverera kuti akanafuna kuti abwere mu mzere wa pemphero. Kapena, ife tikhoza kuwagwiritsa ntchito ena a iwo kanthawi kena, mu usiku, kwa mzere wa kuzindikira zamumtima. Ndi. . . Nchomwe chiri. . .

⁴ Si kuzindikira zamumtima kumene kumamuchiritsa munthu. Iko kumangowayika iwo mu chikhalidwe kuti aziyang'ana mmwamba ndi kulandira machiritso awo amene Yesu anawachitira kale iwo. Mwaona? Kuyika kwa manja ndi chinthu chabwino kwambiri, chifukwa n—ndi cha Mwamalemba. Koma si njira ya Amitundu yochiritsidwira.

⁵ Umu, mu Baibulo, munali Myuda yemwe anali naye. . . Mwana wake wamkazi yemwe ankadwala kwambiri, pafupi kufa, ndipo iye anafa. Ndipo iye anati kwa Yesu, “Mwana wanga wamkazi wagona, pafupi kufa, koma bwerani ndi kudzayika manja Anu pa iye, ndipo iye achiritsidwa.”

⁶ Koma pamene kenturio, wa Chiroma, Wamitundu, pamene wantchito wake anadwala, iye anati, “Ine siwoyenera kuti Inu mubwere pansi pa denga langa. Ingoyankhulani Mawu.” Ndi chimene chinatembenuza mtima wa Yesu. Sanachite kusowa kuti ayike manja pa iye. Iye ankangofuna kuti amve Mawu.

⁷ Inu mukuona, ine ndimaikonda nkhani imeneyo. Chifukwa, wa Chiroma uja anazindikira kuti iye anali mwamuna wa ulamuliro. Ndipo ngati iye anena kwa munthu, “chita *ichi*” kapena “chita *icho*,” iye ankachita izo. Ndipo iye anazindikira ulamuliro uwo womwe, ulamuliro mwa Ambuye Yesu. Chifukwa,

i—iye ankadziwa kuti ngati iye akananena kwa munthu yemwe ali pansu pa iye, “iwe pita” kapena “iwe bwera,” iye anka-yenera kuti azimumvera iye.

⁸ Ndipo iye ankadziwa kuti zodwala zonse ndi matenda zinali pansu pa ulamuliro wa Ambuye Yesu, chotero Iye sankasowa kuti achite kubwera, kudzayika manja pa wantchito. “Ingoyankhulani Mawu, ndipo wantchito wanga akhala moyo.”

⁹ Ndipo Yesu anazizwa, ndipo Iye anati, “Ine sindinapezepo chikhulupiriro chonga icho mu Israeli.”

¹⁰ Kotero, ine ndithudi ndikuyembekeza kuti ine ndikhala moyo mpaka ndidzaliwone tsiku limene ife Achimereka titi tidzakhale nacho chikhulupiriro cha mtundu uwo. “Ingoyankhulani Mawu, Ambuye, ndipo wantchito wanga akhala moyo.” O, ilo lidzakhala tsiku lalikulu. Tsopano ife tiri. . .

¹¹ Nthawizina pamene kudzoza kuli kolemera kwambiri, ndipo nthawizina ine sindimapeza mwayi woti ndipange kuyitanira paguwa. Ena a abale ena, M’bale Sullivan kapena ena a abale anga opambana muno, amasamalira zimenezo.

¹² Winawake akhoza kunena kuti ife timangokokomezera machiritso Auzimu. Machiritso Auzimu angokhala ngati kupita kokawedza. Iwe sumaisonyeza konse nsomba mbedza. Iwe umangoisonyeza iyo nyambo, ndipo iyo ikavumbata nyamboyoy ndipo imapeza mbeza. Kotero, umo ndi momwe ziliri ndi machiritso Auzimu. Ndi okopa chifukwa i—iwo amawonetsera ndi kutsimikizira kuti alipo Mulungu yemwe alimoyo ndipo akukondweretsedwa ndi inu. Ndipo wosakhulupirira akawona izo, mwamsanga diso lake limagwira izo ndipo amadziwa kuti alipo Mulungu wamoyo, ndiyeno iye amakhala pa mzere wa chipulumutso apono. Mulungu akhoza kupita nakumulamulira iye ndiye, ndi kumulowetsa iye umo. Kotero, ndicho chimene machiritso Auzimu aliri, basi kwa cholinga chimenecho.

¹³ Anyamatawa muno ali nawo matepi ena, ndi mabuku, ndi marekodi, ndi zina zotero, zomwe iwo ali nazo malonda apang’ono a iwoeni omwe iwo amawasamalira. Ife sititero. . . Kwa inendekha, ine ndiri ndi mabuku awo okha, ndipo ena a iwo ine ndimachita kuwagula. Alipo ena a iwo omwe ali anga, ulaliki. Enawo ndi mabuku omwe ine ndimawagula kuchokera kwa M’bale Lindsey, otchedwa *Mbiri Ya Moyo Wanga*. Ndiyeno liripo lina lotchedwa *Mneneri Achezera Afrika*. Ndi—ndipo ine ndikukhulupirira atatu kapena maulaliki anayi ndi anga. Iwo ali nawo uko, osati pofuna ndalama, kungoti kuti Uthenga uzifika kwina.

¹⁴ Ndicho chinthu chachikulu, kuufikitsa Uthenga kwina, pakuti ife tikukhala mu ora mochedwa kuposa momwe ife tikuganizira. Tiri pa kutseka kwa m’badwo, ndipo mpingo uli mu chikhulidwe chowopsya, ndipo ife tiri kungoyesera

kumwaza kuwala kwa dzuwa pakati pa anthu. Osati kuyesera kuti tiwatembenezire iwo ku zikhulupiriro zathu zina, koma kuti tiyesere kuwatengera iwo kuti azikhala moyo pafupiko ndi Ambuye Yesu ndi kuti azimukhulupirira Iye; osati kuti tikoke mamembala kuchokera ku mpingo, kupita ku mpingo wina; koma, kuti titumize mamembala ena ku mpingo umenewo, ndicho cholinga chathu.

¹⁵ Tsopano...ife tisanati titsegule kumene Mawu, kwa Uthenga wa madzulowa, umene uli wawufupi. Ife sitikufuna kuti tikusungeni inu motalika, chifukwa ambiri akuchokera kutali ndi mzinda, ndipo inu muyenera kuti mukabwerere ku ntchito. Ndipo ife tiyembekezera mpaka Loweruka usiku, ndi kudzakusungani inu mochedwa pamenepo. Ndiyeno, Lamlungu, inu simudzasowa kuti mudzapite ku Sande sukulu mpaka hafu pasiti naini.

Kotero tiyeni ife tiweramitse mitu yathu mphindi yokha, kwa mawu a pemphero.

¹⁶ Ambuye, ife tiri oyamikira, kupitirira lingaliro, chifukwa cha mwayi wa kubwera ndi kudzaweramitsira mitu yathu kwa Mulungu wamoyo, ndi kudziwa kuti ife tinalonjezedwa kale, ndi Mwana Wake woyera, Ambuye Yesu, kuti ife tikhoza kukhala nazo zomwe ife tipempha, ngati ife tiwapempha Atate mu Dzina la Ambuye Yesu, Mwana Wake. Ndipo ife tatsimikiziridwa kuti ife tidzakhala nako kuyankhulana kapena kukambirana ndi Iye, ngati ife tibwera mu Dzina la Yesu, chifukwa Iye anati, “Apempheni Atate chirichonse mu Dzina Langa, Iye adzachipereka icho.”

¹⁷ Ndipo ife tikutsimikiza mwamtheradi, usikuuno, kuti Iye akutimva ife, ndipo kuti zomwe titi tipemphe ziperekedwa, chifukwa ife tikumverera kuti kupempha kwathu kuli chifuniro cha Mulungu. Chifukwa Iye ananena, mu malo ena, “Inu mulibe, chifukwa inu simumapempha. Ndipo inu simumapempha, chifukwa inu simumakhulupirira.” Ambuye, chifukwa chomwe ife tikudzera ndi chifukwa ife timakhulupirira kumene. Ndipo ife tikukhulupirira kuti Inu mutiyankha. Ndipo mapemphero a—athu si oti angomvedwa ndi anthu, koma ife tikukhulupirira kuti Inu mukumvetsera, ndipo tikutsimikiza kuti Inu mutiyankha ife chifukwa Inu munalonjeza kutero. Ife tingopempha kuti kufuna Kwanu kokha kuchitidwe.

¹⁸ Mulole zikhale, usikuuno, Ambuye, kuti wochimwa aliyense yemwe ali muno, yemwe sakukudziwani Inu ngati Mpulumutsi wawo, mulole uno ukhale usiku umene chinachake chiti chichitidwe kapena kunenedwa, kuti iwo akulandireni Inu monga Mpulumutsi wawo.

¹⁹ Mulole iwo opanda Mzimu Woyera, usikuuno, omwe akulifuna ndi kuliyembekezera ora limenelo pamene makhungu ati adzagwe kuchokera mu maso awo ndipo apo chokhumba cha

mtima wawo chidzaperekedwa kwa iwo, O Ambuye, mulole Mzimu Woyera, usikuuno, udzaze mtima uliwonse. Mulole kuti pakhale kuwonetsera kotero kwa Mzimu wa Mulungu, mpaka miyoyo yawo ikhale yokondowedzedwa kwambiri, mpaka kukaikira kwawo konse ndi zamatsenga zichotsedwe kwa iwo, ndipo Mzimu Woyera ubwere mu moyo wawo ndi kuwasindikizira iwo mu Ufumu wa Mulungu.

²⁰ Perekani, usikuuno, Ambuye, kuti pasakhale munthu mmodzi wodwala pakati pathu, pamene msonkhano uzitha. Mulole aliyense kuti achiritsidwe. Ife sitingati tiwaiwale iwo omwe ali mu zipatala, ndi otsekeredwa, ndi mu ndende, omwe mwakuya akusowa chifundo Chanu. Mukhale nawo iwo, O Ambuye.

²¹ Ndipo pamene ife tizichoka, usikuuno, mulole ife tizinena, monga ophunzira, “Ife taona zinthu zachilendo lero,” ndipo mulole mitima yathu iyake mkati mwathu pamene ife tizipita kwathu kosiyana.” Ife tikudalira pa Inu, Mpulumutsi wathu, kuti mupereke zinthu izi kwa ife molingana ndi lonjezo Lanu. Ndipo lonjezo Lanu nthawizonse ndi chifuniro Chanu. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

²² Ngati inu mukufuna kuti mutembenuze usikuuno mu Zolembedwa zopatulika, ku Bukhu Loyamba la Akorinto, mutu wa 11, ife tikufuna tiwerenge gawo la Lemba, kuyambira ndi ndime ya 23.

Pakuti ine ndinalandira kwa Ambuye chimene inenso ndinachipereka kwa inu, Kuti Ambuye Yesu usiku womwewo momwe iye anaperekedwa, anatenga mkate:

Ndipo pamene anayamika, iye anaunyema iwo, nati, Tengani ndi kudya: ili ndi thupi langa, lomwe lanyemeredwa chifukwa cha inu: ichi muzichita mwa chikumbutso cha ine.

Kenako mwa kachitidwe komweko...iye anatenga chikho aponso, ndipo pamene iye anapereka mayamiko, kuti, Ichi ndi chikho cha pangano latsopano...nthawizonse inu mukamamwa icho, mmwa chikumbutso cha ine.

Pakuti nthawizonse pamene inu mudya mkate, ndi kumwera chikho cha Ambuye, inu muzisonyezera imfa yake kufikira akadza iye.

Chifukwa chake yense amene akadya mkate uwu, . . . namwera chikho cha Ambuye, mosayenera, adzakhala wochimwira thupi ndi mwazi wa Ambuye.

²³ Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwerenge...mutu wanga, kuchokera pa twente- . . . pa ndime ya 29.

Pakuti iye amene adya ndi kumwa mosayenera, . . . adzakhala wochimwira thupi la Ambuye.

24 Tsopano, dikirani. Ine ndaziwerenga izo molakwitsa.

Pakuti iye amene adya ndi kumwa mosayenera, . . . osalizindikira thupi la Ambuye.

. . . adzimwera kwa iyemwini chiweruzo, *posalizindikira* thupi la Ambuye.

25 Ine ndinalirira pa Baibulo ili, ndipo ilo liri ndi malo ena osaoneka mwa ilo.

26 “Posalizindikira Thupi la Ambuye.” Tsopano, phunziro langa usikuuno ndi: *Kulizindikira Thupi La Ambuye*.

27 Tsopano, kopitako kwathu Kwamuyaya sikuti kwathunthu kumatsimikizika ndi zomwe ife timaziwona ndi zomwe ife timazimva, koma kumatsimikiziridwa pa kuzindikira kumene ife tiri nako pa zomwe ife timaziwona ndi zomwe ife timazimva.

28 Paulo sanali kutsutsana nawo iwo chifukwa chotenga mgonero. Machitidwe awo anali olondola, koma kuzindikira kwawo kunali kolakwika. Pakuti, kutenga mgonero wa Ambuye ndi langizo la Ambuye, koma kutenga iwo mosayenera, mosalizindikira Thupi la Ambuye, ndi pamene kulakwitsa kwagona. Akhristu awa anali kutenga mgonero ndi kusamakhalala moyo. Chikhristu ndicho chokuchitikira ndi moyo. Ndipo Akhristu awa ankangokhalala moyo wa mtundu uliwonse, kumapanga chitsanzo chosauka cha kudzinenera kwawo. Ndipo Paulo akunena, kuti, “Pachifukwa ichi, ambiri ali odwala ndi ofooka pakati panu, ndipo ambiri ali kugona,” chimene chikutanthauza ali akufa, “chifukwa iwo sanalizindikire Thupi la Ambuye.”

29 Ndipo ife omwe timadzitcha tokha Akhristu, tiribe ufulu kuti tizitenga mgonero kupatula tiri tikukhala moyo wopanda chitonzo cha mdziko. Ife tiribe ufulu. Mgonero ndi wa iwo amene akukhala moyo woyenera, monga chitsanzo cha Chikhristu. Chinthu choyipisitsa chimene chiripo mu dziko ndi munthu kuyesera kutsanzira chinachake, ndipo ziripo zochulukira kwambiri za izo mu dziko lero.

30 Ife sitiri kokha, mu tsiku lino, ochimwira mulandu womwewo umene Paulo anali kuwudzudzulira mpingo waku Korinto, koma pakuyesera kuchita chinachake chimene Ambuye anali atalamulira, mopanda kulizindikira Thupi la Ambuye. Ndipo Thupi la Ambuye ndi okhulupirira.

31 Koma, lero, ife tikumachita zinthu, mopanda kuwazindikira Mawu aliwonse a Mulungu. Ife tiyenera tizikhala nako kuzindikira pa chirichonse chimene ife tikuchichita. Icho chiyenera kumayezedwa ndi Mawu a Mulungu. Zonse zomwe Akhristu akuchita ndi kunena ziyenera ziziyezedwa ndi Mawu a Mulungu.

32 Lero, anthu asintha pang’ono ndithu, ndipo iwo nthawizina amaika kudalira kochulukira pa chimene mpingo unena kuposa

zomwe Mawu anena. Iwo amakhulupirira, ndiye, kuti mpingo uli nawo ufulu wabwinoko kuti uzizindikira zofuna zathu kuposa zomwe Mawu a Mulungu aliri. Mwa chitsanzo, monga ichi, mpingo ukhoza kunena, “Masiku a zozizwitsa anapita.” Ndipo anthu ambiri amakhulupirira izo chifukwa iwo akuganiza mpingo umadziwa zochulukira za Iwo kuposa Mzimu Woyera umene unalembe Mawu’wo. Chotero, ife sitiri kukhoza kuzindikira zinthu za Mulungu.

³³ Yesu ananena nthawiyina, kuti, “Kupatula munthu atabadwa kachiwiri iye sangakhoze kuwuwona Ufumu wa Mulungu, kapena kuwumvetsa.” Ndipo mwa kuyankhula kwina, “Iwe sungakhoze kuuzindikira Ufumu wa Mulungu mpaka iwe utabadwa kachiwiri.”

³⁴ Anthu amene angabwere ndi kumatiuza ife kuti, “Iwo amene avomereza chokuchitikira cha ubatizo wa Mzimu Woyera,” kuti, “iwo ali otentheka.” Kapena, “Iwo ali a dzina lina losakhala laumulungu,” limene Mdierekezi analimatika pa Mpingo, kuti aziwacha iwo “oyera-odzigudubuza.” Ine ndalalikira mu dziko lonse, ndipo ine sindinayambe ndamuwonapo woyera wodzigudubuza panobe. Ndi dzina lomwe Mdierekezi analimatika pa Mpingo wa Mulungu wamoyo. Nthawizina anthu samakhala nako kuzindikira koyenera. Iwo amaziwopa Izo.

³⁵ Kodi inu simukudziwa kuti Ambuye wathu ananyozedwa pagulu-...ananenedwa kuti ndi munthu wopenga? Afarisi, mpingo wapamwamba, anati, “Munthu uyo wasokonezeka mutu Wake. Iye ali ndi mdierekezi, ndipo Iye ndi wamisala.” Ndipo mawu akuti *misala* amatanthauza “kukhala wopenga.” Ndipo ngati iwo anamutcha Iye “wopenga,” mmochulukira bwanji angawatche amene ali ophunzira Ake?

³⁶ Paulo ananena kwa Agrippa, “Mu njira yomwe izo zikutchedwa *zosokonezeka*, ‘kupenga,’ ndi momwe ine ndikumupembedzera Mulungu wa makolo athu.” Ndine wokondwa kwambiri usikuuno kugwirana chanza ndi iye. Mu njira yomwe izo zikutchedwa “zotentheka,” kwa mpingo wamakono, ndi momwe ine ndikumupembedzera Mulungu. Iwo ankatchedwa “otengeka,” chifukwa iwo sankalizindikira moyenera Thupi la Ambuye, ndiwo, Mpingo wa Mulungu wamoyo.

³⁷ Ndipo Mpingo, usikuuno, ukutchedwa “wopenga” chifukwa anthu alibe kuzindikira. Ngati munthu wabadwa kachiwiri, ndipo inu mukufuna kundiuza ine kuti inu munabadwa kachiwiri, ndipo inu simukukhulupirira kuti machiritso Auzimu ndi lonjezo la Mulungu, ndipo inu simukukhulupirira kuti ubatizo wa Mzimu Woyera ndi woyenera kwa anthu lero, ndiye ine ndiyenera kunena kuti kubadwa kwanu kunali kwa mzimu wolakwika.

38 Chifukwa, Mzimu Woyera unanena, kuti, “Lonjezo ili liri kwa inu ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo omwe ali kutali, ngakhale onse omwe Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.”

39 Inu mukulandira izo mwa lingaliro laluntha. Anthu akumatenga mawu a munthu winawake mmalo mwa izo, ndipo alibe kuzindikira. Iwo sangakhoze kuzindikira pakati pa chokhoza ndi cholakwika.

40 Ine ndikuganiza, lero, kuti, ambiri a ife zimphona zaluntha; osati ife, koma zimphona zambiri zaluntha. Anthu a Mulungu sanayambe akhala aluntha aakulu. Baibulo linanena, kuti, “Ana a mdima ndi anzerupo mu dziko lino kuposa ana a Kuwala.”

41 Mulungu amawafanizitsa anthu Ake kwa nkhusa. Iwo si anzeru ndi aluntha. Iye amawasunga iwo momwe iwo aliri kotero Iye azikhoza kumawatsogolera iwo. Ngati inu muyesera kuti muzigwiritsa ntchito kuganiza kwanu kwanu kwaluntha, inu mukhoza, apo pomwe inu mukumutchinga Mulungu. “Ana a Mulungu amatsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu.”

Koma ndi tsiku lalikulu laluntha limene ife tiri kukhalamo.

42 Kuno, miyezi ingapo yapitayo, inu munaziwerenga izo mu nyuzipepala. Uko mu New York, iwo anali n—ndi mulandu. Ndipo alaliki awiri aang’ono omwe anamverera kutsogozedwa ndi Ambuye, nthawiyina pakale; anthu aang’ono apafupi ngati inemwini, omwe sankadziwa nkomwe ABC wawo. Ndipo Ambuye anawatsogolera iwo ku Bowery. Ndipo iwo anagula nyumba inayake, ndipo iwo anali kulalikira Uthenga umo kwa abale awo okugwa. Kampani ina yaikulu inabwera kuti idzaigule iyo. Ndipo onse awo anagulitsa, koma alaliki aang’ono awa. Iwo anali ndi vumbulutso kuti Ambuye amafuna kuti iwo atsalebe uko, kotero iwo anagwira malo awo.

43 Ndipo aulamuliro anawabweretsa iwo mu khoti. Ndipo iwo anatumiza nakampeza mmodzi wa zimphona zazikulu zaluntha, Woimiramlandu Greenwall, ndipo iye anawapangitsa anyamata aang’ono awo kudzichitira manyazi okha. Iye anawayika mawu ake mokhoza kwambiri ndi kwambiri moga mwamaphunziro, ndi mwa njira yakuti anyamata aang’ono awo sankadziwa momwe akanamuyankhira iye. Pakuti, iye anali chimphona chaluntha, mmodzi wa oyimira mulandu abwino kwambiri omwe alipo mu...mu New York. Ndipo iwo anawasokoneza anyamata aang’onowo, mwakuti iwo sankadziwa choti anene. Potsiriza, iye anagogoda nati, “Inu mungadzinere chiani panokha?”

44 Ndipo mmodzi wa azilaliki aang’onowo anawuka, ndipo anagwira manja a winayo, ndipo iye anati, “Bwana, chinthu chokha chimene ife tikuchidziwa, nkuti Ambuye anatiuza ife kuti tiyitenge nyumbayi.”

45 Ndipo Woimiramlandu Greenwall anati, “Muno, siyani izo. Ife sitikufuna Ambuye ayi pa mlandu uwu.”

46 Pafupi masabata awiri kenako, ndege inkayesera kuti idutse pansu pa mlatho, ndipo iyo inagwera mmadzi achisanu. Ndipo apo Woimiramlandu Greenwall, anali mmadzi, akuvutika ndi kufa. Ine ndikudabwa ngati iye anamufuna Mulungu pa malo amenewo.

47 Kodi vuto linali chiani? Iye sanalizindikire Thupi la Ambuye, chifukwa alaliki aang’ono awo anali atadzedwa ndi Mzimu Woyera ndipo anali nacho chifuniro cha Mulungu. Iye sitimasowa kuti tizikhala zimphona zaluntha. Iye tikusowa kuti tikhale antchito odzichepetsa a Ambuye, ndi kumalizindikira Thupi Lake. Ndipo kuphunzira kwake konse, ndi kuthyathyalika kwake, ndi maphunziro ake? Inu mukudziwa, Baibulo linati, “Ndi kwabwino kwa inu kuti mphero ikanati ipachikidwe pa khosi panu, ndipo inu kuti mumizidwe mu kuya kwa nyanja, kuposa kuti mukhumudwitse odzozedwa Anga.” Ine ndikuganiza kuti iye anali nayo nthawi yochulukira yoti alingalire za kuwaitanira Ambuye pa malowo, koma iye sanalizindikire Thupi la Ambuye.

48 Nthawizina ine ndimadabwa ngati ife Achimereka aluntha tiri nako kuzindikira kokwanira kuti tizizindikira chokhoza kwa cholakwika. Makamaka mabwalo amilandu achinyamata akutsimikizira kuti ife tiribe izo kuti tizizindikira chokhoza kwa cholakwika, kwa ana athu, ndipo iwo akuwoneka kuti ali ndi yankho labwino lawowerenga maganizo.

49 Mwa chitsanzo, monga chonchi. Ngati mwana abwera kwa abambo ake nadzamenyetsa phazi lake laling’ono, ndi kumalira ndi kupukusa mutu wake, nkuti, “Adadi, ine sindikusamala zomwe inu munganene. Ine ndikufuna ndodo yamagetsi.” Ndizo zenizeni za Amereka.

Ndipo bambowo amati, “Chabwino, mwananga, ine ndikakugulira iwe iyo.”

Inu mukhoza kunena kwa bambo awo, “Nchifukwa chiani inu munachita izo?”

“O, ine ndimamukonda iye.”

50 Inu mukumbukire, adadi, mwananuyo adzakula kuti adzakhala bambo, tsiku lina, ndipo iye adzakwatira ndi kudzakhala ndi banja. Mulungu amuthandize mkazake uyo yemwe akukhala ndi mnyamata yemwe waleredwa monga choncho, kuti azikhala nazo mwanjira yake zonse zomwe iye azifuna. Sangakhoze kuzindikira chokhoza kwa cholakwika. Icho si chikondi. Uwo ndi umbuli weniweni. Baibulo ndi lokhoza. “Mukasunga ndodo, ndipo inu mumuwononga mwana wanu.”

51 Fanny wamng’ono angabwere kwa amake, ndipo iye akuti apite ku kwasakwa. Amake akamuuzza iye kuti sangakhoze kuchita izo. “Koma, o, amayi, ndinu wankhanza kwa ine.” Ndithudi, inu mumamukonda Fanny, ndipo inu mumamulola

kuti iye apite. Iye akafika pakati pa gulu ilo la zigawenga, pa zamkutu zonse izo; kubwera kunyumba, ndi kuwonetsa milomo yake yolochedwa ndi kukuuzani inu bodza, kuti, “Palibe chowononga mu ilo.” Mulungu amchitire chifundo mwamuna yemwe ati adzakwatire chinachake chonga icho kukhala mkazake. Kuzindikira chokhoza kwa cholakwika, ife sitingakhoze kuzizindikira zathu zomwe.

⁵² Ine ndimadabwa nthawizina ngati ife tingakhoze kuzindikira chokhoza ndi cholakwika, kwa matupi athu omwe, makamaka Thupi la Ambuye. Ife sitikuzindikira chokhoza ndi cholakwika, pa matupi athu omwe. Tsiku ndi tsiku, ndi sabata ndi sabata, mwezi ndi mwezi, ndi chaka ndi chaka, azasayansi akumagwira ntchito mu nyumba zopimira, ndi kuyika zilembo zazikulu panja, ndi chirichonse, ndi zolengeza, ndi kumawachenjeza anthu, “Khansara mu katoni.” Amuna, masauzande thuu handiredi ndi sevente chinachake Achimereka afa chaka chino chifukwa chosuta ndudu, ndipo inu mukumasutabe. Inu simukukhoza kuwazindikira ngakhale matupi athu omwe, ndiye mukanena za kuuzindikira Mzimu Woyera ndi mu Thupi la Ambuye.

⁵³ Kodi inu munaiwona nkhani ija tsiku lina, yomwe sayansi iyi inatulutsa, zofufuza zake zonse? Iye anati, “Osati ndudu zokha, kuti zimakupatsani inu khansara, koma inu muli nawo mwayi wa magawo fifite pa zana wa kutenga china chirichonse.” Ndipo inu mukumasutabe.

⁵⁴ Mkazi anakomana nane ine, nthawi yina pakale, pamene ine ndinakhudza pa izo molimba basi monga ine ndikanathera. Iye anali wosuta mwachizolowezi. Ndipo iye anati, anayika cholemba chake chaching’ono mthumba mwanga, anati, “Mukawerenge izo pamene inu mukafika kwanu.”

⁵⁵ Ine ndinati, “Zikomo inu. Ine ndiziwerenga izo tsopano.” Ndipo ine ndinakatulutsa iko ndi kuyamba kukawerenga.

⁵⁶ Iye anati, “Si chaulemu kuti mtumiki pa guwa aziyankhula motsutsa kusuta. Iwe ulibe kanthu kochita nazo.”

⁵⁷ Ine ndinati, “Ndi ntchito yanga kuti ndiziyankhula motsutsa chirichonse chomwe chiri cholakwika.”

⁵⁸ Mulungu amthandize mlaliki yemwe alibe kuzindikira kwa chokhoza, mokwanira, kwa chirichonse chomwe chiri cholakwika; mlaliki yemwe sangakhoze kuzindikira chosowa cha anthu ake, mwa Mzimu Woyera. Mulungu anati, “Thupi ili ndi kachisi wa Mzimu Woyera. Ngati inu muliyipitsa ilo, Ine ndidzaliwononga ilo.” Ife tiyenera kumalalikira motsutsa izo. Vuto lake ndi lakuti, ife tiri nawo alaliki ochuluka kwambiri osuta ndudu. Ndiyo yomwe ili nkhani. Ndipo iwo amawopa kuti azinena izo mwa osonkhana awo, chifukwa iwo amadziwa kuti ali olakwa, nawonso.

“Kulizindikira moyenera; kugawaniza moyenera.”

⁵⁹ Akachaso, mowa, bwanji, iwo amati, “Ndi zokupweteka.” Ponseponse pa kanema wa televizioni,ponseponse pa chikwangwani chirichonse, mu nyuzipepala zanu, pali zitini zazikulu za mowa pali asungwana okondeka akuumwa iwo. Iwo amakusonyezani inu pamene iwo akuyambira. Muziyang’ana pa iwo mtsogolo pang’ono kuchokera apo. Iwo umadzazitsa malingaliro awo ndi ndulu ya chiphe. Kuchulukitsa kwake kwa misala ndi kowopsya. Iwo umayambitsa makhalidwe oipa pakati pa achinyamata.

⁶⁰ Ndipo ngakhale mipingo, lero, ikulalikirana ndi kumazichita, ochuluka a iwo, “Muzimwa mwapang’ono.” Inu mukudziwa kuti izo ndi zoonaa. Kumawauza achinyamata awo kwawo, ndi makolo, “Muziwalola ana anu azimwa. Iwo adzamwabe, mulimonse, kotero inu muzingowaphunzitsa iwo kuti azimwa mwapang’ono.” Baibulo limatsutsa izo. Si zolondola. Mulungu amuthandize munthu wopanda kuzindikira kuposa izo, kapena mpingo, wosakhoza kuzindikira chokhoza kwa cholakwika. O, ndi tsiku lowopsya limene ife tiri kukhalamo.

“Kulizindikira Thupi la Ambuye.”

⁶¹ Mu mipingo yathu, ndi pakati pa anthu a mpingo wathu lero, ndi chamanyazi chotero, momwe akazi athu akumachitira, nawonso. Ambiri a iwo kumavala zovala mopanda khalidwe, akabudula aang’ono awo. Ndi chochimwa kwambiri. Dona anandiuza ine, ndi ambiri anandiuza ine, kuti, “Billy, iwe kulibwino usiye kuyankhula za izo.” Ayi, bwana. Ine ndikhoza kumalalikirana kwa mizati, koma ine ndidzakhala ndikunena Choonadi. Ndiko kulondola. Ndiko kulondola. Ndicho Choonadi. [Osonkhana avomereza—Mkonzi.] Zikomo inu. Ndi cholakwika ndipo ndi chatchimo kwambiri.

⁶² Alipo dona mmodzi ananena kwa ine, iye anati, “Ine sindimavala akabudula. Ine ndimavala matrauzi.”

⁶³ Ine ndinati, “Izo ndi zoipisitsa. Baibulo linati, ‘Ndi themberero kwa Mulungu, kuti mkazi azivala chovala chimene chiri choyenera kwa mwamuna.’” Ndi Choonadi.

⁶⁴ Ndiyeno chowiringula chake nkuti, “Iwo sakumapanga zovala zinanso kupatula izo.” Koma iwo akupangabe makina osokera ndipo akugulitsa nsalu.

⁶⁵ Mkazi yemwe amadziveka yekha monga choncho, iye adzakhala ndi mulandu wa chigololo, pa Tsiku la Chiweruzo. Iwe ukhoza kukhala wangwiro ngati kakombo, kwa mwamuna wako kapena bwenzi lako lachimuna. Koma Yesu anati, “Aliyense yemwe ayang’ana pa mkazi kuti amusilire iye wachita kale chigololo ndi iye mu mtima mwake kale.” Kotero, iwe ukhoza kukhala kuti sunachitepo chirichonse cholakwika mwakuchita. Koma pamene iwe unadziveka wekha monga choncho, iwe unadzipereka wekha kwa mwamuna; iye adzayenera kuti adzayankhire pa kuchita chigololo, ndipo

wolakwa ndi iweyo. Ndipo mpingo ukuloleza izo, posalizindikira Thupi la Ambuye. Ndi chachisoni bwanji!

⁶⁶ Kumadula tsitsi lawo. Baibulo linanena, kuti, “Mkazi yemwe adula tsitsi lake, mwamuna wake ali ndi ufulu womusudzula iye,” chifukwa iye ndi wosawona. Iye ananena, kuti, “Iye akunyozetsa mutu wake.” Kodi ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] “Ndipo mwamuna ndiye mutu wa mkazi.” Ine ndikudziwa kuti izo ndi zolimba, koma ife tikusowa kuzindikira.

⁶⁷ Ife tikusowa kuti tizizindikira izo mwa Mawu. Mawu ndiwo owona. Atengeni Mawu. Mawu a Mulungu nthawizonse ali olondola. Ife sitingakhoze kuzindikira ndi zomwe anthu akuganiza, zomwe aluntha akutiiza ife, zomwe azamisala akutiiza ife. Ife tiyenera kumayendera zomwe Mulungu anena. “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.”

⁶⁸ “Posalizindikira Thupi la Ambuye; ambiri ndi ofooka ndi odwala, ambiri agona, afa, afa mwauzimu.” Mliri wotsiriza umene unakantha Igupto unali imfa. Mliri wotsiriza umene wakantha mpingo ndi imfa yauzimu. Chimene ife tikusowa lero ndi kudzutsidwa kwauzimu, kudzutsidwa kwauzimu, kuti tizizindikira.

⁶⁹ Anthu awa akhoza kukhala kuti amachita izi, o, ndi zolinga zabwino.

⁷⁰ Bambo uja Kummwera uko, dotolo uja tsiku lina, yemwe anamupatsa munthu uja asidi wa salfa chimene chinamupha iye. Iye anali ndi zolinga zabwino. Iye ankaganiza kuti anali kulondola, koma iye anali ndi kuzindikira koperewera. Iye sanawazindikire mankhwala ake.

⁷¹ Monga msungwana wamng’ono yemwe ankayenda mu msewu, ndipo iye anampeza mphaka wamng’ono, ndipo iye anali atangonyowa yense ndipo anali mwatheka pafupi kugwidwa chisanu. Ndipo iye anamutengera iye mkati, anategula chitseko cha uvuni yake ndi kumuika iye mu uvuni, kuti ampangitse kutenthedwa. Zolinga zake zinali zabwino, koma kuzindikira kwake, kunali koperewera. Bwanji, osati...Ife tikapanda kupenyetsetsa, ife timuphika mphaka, nafenso, ndi kuzindikira kwathu kwina kwaluntha.

Achikominisi akubwera pa ife. Dziko likudza pa ife.

⁷² Mipingo yathu yaphwasuka. “Anthu akudzigawa okha, kudzipatulitsa eniake, osawoneka kuti ali nacho Chikhulupiriro,” kugawaniza tsitsi pa ziphunzitsa zazing’ono zopandapake. Ife tiyenera kumabwera pamodzi, nkono ndi mtima, ndi kupemphera, ndi kusala, ndi kuitana mpaka Mulungu atautumizanso Mzimu Woyera, kuti ife tikhoze kukhala nako kuzindikira kwauzimu.

⁷³ Ora lafika pa nthawi yotsirizayi tsopano, ife tiri mu mithunzi ya Kudza kwa Ambuye, ndipo mpingo sukukhoza kuzindikira izo. Ife tikukhala mu ora lakumapeto kuposa momwe inu mukuganizira.

⁷⁴ Ngati Paulo angakhoze kuwuka kwa akufa, usikuuno, mu Middletown, inu mukayankhula za moto woyaka! Iwo akanamuika iye mu ndende kusanache, ngati “wamisala kapena munthu wolusa.” Munthu uja, atadzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndi kuwona zinthu zikuchitika momwe izo ziriri, ndi podziwa kuti nthawi ili pafupi, pakanati pakhale chitsitsimutso kapena iwo akanati achite kubwera ku ndende kuti adzamumvere iye. Ndiko kulondola.

⁷⁵ Tsopano, o, Yesu anati, ndipo Baibulo likuyankhula izo. “Mu masiku otsiriza, basi kusanachitike Kudza kwa Ambuye, padzakhala pali zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa ziri kuchitika mu dziko lapansi.” Ndipo inu mukudziwa, mpingo uli wakufa kwambiri mu zamulungu, ndi mitundu yonse ya masukulu, ndi kuphunzitsa, ndi mapurogramu a maphunziro, mpaka iwo sukukhoza kuzindikira zinthu zimenezo.

⁷⁶ Kodi Yesu sananene kwa mpingo mu tsiku Lake, “Inu mukumakhoza kuzindikira mawonekedwe a mlengalenga, koma zizindikiro za nthawi inu simukukhoza kuzindikira. Pakuti ngati inu mukadandidziwa Ine, inu mukanalidziwa tsiku Langa?”

⁷⁷ Ora la chiwombolo cha mpingo, ndipo iwo sakukhoza kulizindikira ilo. Ife tiri kwambiri... Chinachake chalakwika. Ine ndikuyankhula za mpingo wonse, aliyense yemwe amadzitcha yekha Mkhristu.

⁷⁸ Mulungu akhoza kuyamba kusuntha, ndipo zinthu zauzimu nkumachitika, anthu nkumapululumutsidwa ndi kumadzazidwa ndi Mzimu Woyera; zikwi zochuluka omwe amadzitcha okha Akhristu amachoka kwa Iwo, ndi kuti, “O, Awo! Awo, Awo ndi oyera odzigudubuzwa.” Inu mulibe kuzindikira kwauzimu.

⁷⁹ Chifukwa, zirizonse zomwe Mzimu Woyera umachita zinalembedwa mu Baibulo. Weruzani zinthu zonse mwa Lemba. Ndi momwe ife timazindikirira, kuti tiwone ngati kuzindikira kwathu kuli kolondola.

⁸⁰ Ngati Baibulo linati, “Yesu ali yemweyo dzulo, lero ndi kwanthawizonse,” ine ndikuzikhulupirira Izo. Ngati Baibulo... Ngati Yesu anati, “Zinthu zomwe Ine ndikuchita inunso muzidzazichita,” ine ndikukhulupirira Izo. Ndipo ngati Baibulo linanena, kuti, “Mzimu Woyera ndi wa kwa kam’badwo kalikonse, onse amene Ambuye Mulungu wathu ati adzawaitane,” ine sindikukhulupirira kuti kugwirana chanza kukutenga malo ake.

⁸¹ Ine ndikukhulupirira Iwo ndi Mzimu Woyera womwewo umene unagwa apowo, kusonyeza zizindikiro zomwezo,

zodabwitsa zomwezo. Umboni wopambana umene ife tiri nawo, kuti ife tiri nao Mzimu Woyera, ndi pamene mzimu wathu uchitirana umboni ndi Mawu.

⁸² Ngati ife tikudzitcha tokha Akhristu ndi kumati ndife odzazidwa ndi Mzimu, ndipo ife tikuwona kuti ubatizo wa Mzimu Woyera uli kutsanuliridwa pa okhulupirira kwa mibadwo yonse, ndipo mzimu wathu nkumatiuza ife “Izo ndi za m’badwo wina,” inu mukulakwitsa. Kulondola.

⁸³ Pamene Baibulo linena kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; ngati mzimu wathu unati, “Ayi, Iye anafa; Iye anapita kale,” pali chinachake cholakwika.

⁸⁴ Yesu anati, “Ntchito zimene Ine ndikuchita inu muzidzazichitanso. Taonani, Ine ndiri ndi inu nthawizonse, ngakhale mpaka ku mapeto a dziko lapansi.” Ndipo ngati mzimu wathu ubwera nuchoka kwa Izo, ife tiribe Mzimu Woyera.

⁸⁵ Chifukwa, Mzimu Woyera ukanati, “Ameni,” ku Mawu aliwonse Iye anawalemba. Tsopano, chidziwitsa chaluntha chimakuchotsa iwe kwa Iwo, koma Mzimu Woyera umati, “Ameni,” kwa Mawu Ake Omwe. Iye ndithudi amatero.

⁸⁶ Ndipo Iye akufunafuna, ndi kusaka, ndi kuyesa kuti amupeze winawake yemwe Iye angakhoze kudziyikamo Yekha. Iye akukhumba kuti apeze izo.

⁸⁷ Musati muganize kuti inu mungakhoze kuutsiriza ubwino Wake. Kodi inu mungakhoze kulingalira, nsomba yaing’ono, yotalika theka la inchi, uko pakati pa Nyanja ya Pacific, ikuti, “Ine ndibwino kuti ndizimwa mosamalira madzi awa; ine angayambe kundithera”? Izo zikanakhala zopusa basi poyesa kumaganiza kuti iwe ungautsirize konse ubwino wa Mulungu. “Pemphani zochuluka kuti zisangalalo zanu zikhale zodzaza.” Mukhulupirireni Mulungu pa chirichonse chimene Iye anachilonjeza. Ndi chanu.

⁸⁸ Aneneri a Chipangano Chakale, Daniele ndi enawo, anati, “Mu masiku otsiriza, kuti, anthu amene akanati azimudziwa Mulungu wawo akanadzachita zochuluka.” Ndilo lonjezo.

⁸⁹ Pamene aluntha ayang’ana pa zochuluka, iwo amati, “O, ndi kuwerenga maganizo. Ndi kupepetula. Ndi kugwira ntchito kwa mdierekezi.”

⁹⁰ Koma Mzimu Woyera umayankha mobwezera, “Ameni, icho ndi Choonadi,” kuzindikira kolondola.

⁹¹ Iwo anazilonjeza izo. Yesu anazilonjeza izo. Yesu anati, “Ntchito zomwe Ine ndikuzichita inunso muzidzazichita, ngakhale zazikulu kuposa izi inu muzidzazichita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate Anga.”

⁹² Paulo analonjeza, kuti, “Mu masiku otsiriza,” mwa Mzimu Woyera, kuti, “mpingo udzagwera kwina,” mamilioni a iwo. “Padzabwera kugwera kwina, pakuti anthu adzakhala

ammutu, amalingaliro apamwamba, okonda zosangalatsa kuposa kukonda Mulungu; ophwanya chigwirizano, otsutsa mwabodza, osadzigwira, ndi onyoza iwo amene ali abwino,” opanda kuzindikira kolondola.

“O,” inu mukuti, “awo ndi achikominisi.”

⁹³ Uyo ndi wotchedwa Mkhristu. Penyani ndime yotsatira. “Okhala nawo maonekedwe aumulungu, koma kumakana mphamvu yakeyo.” Opanda kuzindikira kwauzimu.

⁹⁴ Pamene inu muli nako kuzindikira kwauzimu ndi Mzimu Woyera uli pa inu, inu muli nako kuzindikira kwauzimu. Iwo umati, “Ameni,” kwa lonjezo lililonse la Mulungu.

⁹⁵ Paulo anati masiku awo adzakhalapo. Ife tiri nawo iwo. Iwo ali pano. Iwo ali pa ife. Ndipo ife tikuyang’ana ndi kumaziwona izo. Ife tikuzimva izo kuchokera kulikonse.

⁹⁶ Ndipo kodi ife tikuchita chiani? Izo zikuyenera kumatikokera ife palimodzi. Baibulo linati, “Kudzisonkhanitsa tokha palimodzi, ndipo izo mochuluka pamene ife tikuliwona Tsiku ilo likuyandikira.” Payenera kukhala pali chitsitsimutso chimodzi pambuyo pa china, ndi moto wa ulemerero wa Mulungu utakula mu mpingo uliwonse ndi malo aliwonse. Kubwera palimodzi kwakukululu, kumene mipingo yonse, “Ndi mtima umodzi ndi chiyanjano chimodzi, kudzisonkhanitsa yokha palimodzi,” ndi kuyiwala zamulungu zawo zopangidwa ndi anthu, ndi kumalirira kwa Mulungu pofuna mphamvu yauzimu ndi kuzindikira kwauzimu. Ndilo ora lomwe ife tikulisowa.

⁹⁷ Ine ndikhoza kunena izi, kuti, Yesu watipatsa ife tsikulo, monga ine ndinakhudza pa izo usiku watha, kuti tiidziwe nthawi yotsiriza. Yesu anati, “Monga izo zinali mu masiku a Loti, chomwecho izo zidzakhala ziri mu Kudza kwa Mwana wa munthu.” Tsopano, kodi Mzimu wanu ukuzizindikira izi molondola, “Monga izo zinali mu masiku a Loti”? Kumbukirani, Loti anali choimira cha Amereka. Iye watsimikizira izo. Kodi tchimo la Sodomu linali chiani? Chinali chisokonezo. Ndipo dziko lathu la Amereka ili, akazi adzitsitsa okha mochuluka kwambiri mpaka zilakolako zachibadwa za aamuna zapotozedwa.

⁹⁸ Ine ndinali mu Los Angeles, masabata angapo apitawo, kwa Anthu Achikhristu Amalonda. Ndipo ndinatenga imodzi ya nyuzipepala zawo zodziwika ndipo ndinawona pamene wina wa olemba anati, kuti, “Kupotozeka ndi kugonana kwa amuna kunali kutachulukira magawo twente pa zana mu chaka chathachi.”

Yesu anati, “Monga izo zinali mu masiku a Sodomu.”

⁹⁹ Apolisi, ndi kuphana mnyumba ndi zonse izo, ziri kupitirira basi, nthawizonse, kulekanitsa anyamata, kumakhala limodzi ngati mwamunake ndi mkazake; akazi kumakhala mwa njira

yomweyo. Anasokoneza malingaliro awo, malingaliro awo auve, chifukwa iwo alibe kuzindikira kwauzimu. Zonse zangokhala kusilira ndi uve. Ndipo iwo sakukhoza kudzikhutitsa okha ngakhale wina ndi mzake. Iwo sakukwatira nkomwe. Iwo akumangotengana ndi kumapita kwina, mpaka iwo apotozedwa. Yesu ananena kuti izo zikanadzakhala ziri mu masiku otsiriza, ndipo pano izo ziri.

¹⁰⁰ Ndipo kodi inu muli kukumbukiranso kuti mu masiku a Sodomu. Aliyense, inu mtumiki ndi inu ophunzira Baibulo, ine ndikukhulupirira inu mungavomerezane ndi izi. Dr. Scofield ndi ena ambiri akutero, pafupifupi aphunzitsi onse, Charles Fuller ndi ena otero, masikolala aakulu mu dziko. Kutu, Abrahamu ankaimira Mzimu, Mpingo wauzimu. Loti ankaimira mpingo wachithupithupi, kapena mwachibadwa. Iye anali uko ku Sodomu, mu tchimo. Komabe, iye anali nacho chirungamo mwa iye, koma iye anali akusakanizana ndi izo.

¹⁰¹ Ndipo kumbukirani, uko kunali alaliki awiri aluntha amene anapita uko kuti akalalikire mu Sodomu. Iwo sanachite chozizwitsa; anangowapangitsa iwo khungu. Ndipo kulalikira kwa mtanda kumamupangitsa khungu wosakhulupirira. Ndi chomwe misonkhano yaikulu ya Billy Graham ndi iwo yachita. Iyo yawapanga iwo kuipira.

¹⁰² Pamene Billy Graham, masabata angapo apitawo anachiwona, inu munazimva izo. Kutu, pamene iye anali kuyenda mu England, ndipo iye anachita kumutengera mkazi wake mnyumba, kumchotsa ku maparki, kumene iye anali ndi chitsitsimutso chachikulu, chifukwa amuna ndi akazi anali kuchita zogonana apo pomwe pa gulu poyera kumene iye anali ndi chitsitsimutso.

¹⁰³ Kodi izo zimawachitira ubwino uliwonse? Osati waluntha. Izo zidzatengera kuyitanira-pansi kwa mkwiyo wa Mulungu, ndi Moto Woyera kuchokera Kumwamba, kuti kudzabweretse konse kusiyantsa mu dziko, ndipo izo sizidzakhhalapo. Anthu akuyang'anira mtsogolo ku chinachake chachikulu kuti chibwere, ndipo inu muli pa mapeto a chomwe chabwera kale. Zizindikiro zotsiriza zaperekedwa kwa mpingo wa Amitundu. Ayuda adzakhala nazo Izo Mpingo utakwatulidwa kale. Koma ife tiri pa mapeto a m'badwo wa Amitundu.

Tsopano, potseka pokha, ine ndikhoza kunena izi.

¹⁰⁴ Kodi inu munazindikira kuti ndi Munthu wamtundu wanji yemwe anatsalira mmbuyo, kuti ayankhule kwa Mpingo wauzimu? Anakhala nsana Wake uli ku hema, ndipo Iye ali mlendo. Ndipo anati, "Ali kuti mkazi wako, Sarah?"

Ndipo anati, "Iye ali mu hema."

¹⁰⁵ Anati, "Ine ndidzakuchezera iwe, Abrahamu, molingana ndi lonjezo lomwe Ine ndinakupatsa iwe." Ndipo Iye . . . Sarah, mkatimo, anaseka mwa yekha.

Ndipo Mngelo anati, “Nchifukwa chiani iye waseka?”

¹⁰⁶ Yesu anati, “Monga izo zinali mu masiku a Sodomu, chomwecho izo zidzakhala ziri mu Kudza kwa Mwana wa munthu.” Tsopano kodi inu mukumvetsa? Inu mukumvetsa chifukwa chomwe utumiki wonga uwu ungakhoze kokha kumapita kwa anthu a Uthenga-wonse? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mukuona pomwe izo zafika? Ine ndinaleredwa mu mpingo wa Baptisti, ndipo ndinadzedwa mlaliki wa Mishonare Baptisti. Koma pamene Chinachake chinakhudza mtima wanga, ine ndinali nako kuzindikira kuti Awo anali Mawu a Mulungu, ndipo Iye anawapangitsa Iwo kuwonetseredwa.

¹⁰⁷ Iwo anandiuza ine, “Iwe ukhala woyera wodzigudubuza, Billy. Palibe wina ati azidzamvetsera ku zinthu zotero monga Izo.”

¹⁰⁸ Ine ndinati, “Ngati Mulungu wazitumiza Izo, Mulungu anazilonjeza Izo mu Baibulo Lake, Iye adzakhala naye winawake woti azidzamvetsera kwa Izo.” Ndiko kulondola.

¹⁰⁹ Tiyeni tizilindikira Thupi la Ambuye, tiziizindikira nthawi zomwe ife tiri kukhalamo. Ife tifa, mwauzimu, ngati ife sitichita izo. Ndipo ngati izi ziri zooni. . . Ndipo Mzimu Woyera uli nafe, ndipo ife tiri nacho chizindikiro chotsiriza cha Kudza kwa Ambuye, basi kusanachitike kudza Kwake. Kumbukirani, izo zinali basi Sodomu asanawotchedwe, maora ochepe okha iye asanawotchedwe. Ine ndikukhulupirira, lero, ambiri. . .

¹¹⁰ Inu nonse munamva zomwe Krushchev ananena tsiku lina, kwa Achimereka. Inu munaziwerenga izo mu mapepala anu. Kunena kwake kunali uku. Inu muli nako kuzindikira kwa chibadwa, inu mukazimvetsa izi. Iye anati, “Ngati alipo Mulungu, Iye aseska kachisi ndi kumuyeretsa iye, ndi ukapitolositi wanu wosinthanitsa-ndalama.” Inu mukuona chomwe izo zikutanthauza, sichoncho inu? Ndipo iye akulondola. Wachikunja, mdierekezi, wonyengezera monga uyo, ayenera kukuponyerani apo kuwopsyeza.

¹¹¹ Komabe, iwo akumagona, kumachimwa, kumamwa, osalabadira basi, chifukwa iwo alibe kuzindikira kwauzimu pa Thupi la Ambuye. Tsiku lake limene ife tiri kukhalamoli!

¹¹² M’bale ndi mlongo, kwa inu okonedwa anganu, ine sindiri kuyesera kuti ndikondere. Ine ndikungokuuzani inu Choonadi. Ine ndi woti ndidzayankhire kokha kwa Baibulo. Ndipo ine ndikukuuzani inu, ngati inu mukupitirira kukhulupirira mwa ine kuti ndine mneneri Wake kapena wantchito Wake, inu mukhulupirire kuti ine ndikukuuzani inu Choonadi. Mapeto ali pafupi. Pafupi motani, ine sindikudziwa, ndipo palibe munthu winanso yemwe akudziwa. Koma ine ndikudziwa ife tikukhala mu mithunzi ya Kudza Kwake.

Kodi inu simukuwona kuwopsyeza uko? Inu mukuona zomwe iwo ali nazo.

¹¹³ Fuko likuyesera kuti lizichotse pakumwa, kuzichotsa pakuseka. Inu simungakhoze kuchita izo. Iwo akuchita izo, pothawa kuti atenge kuzindikira kwauzimu kumene Mulungu angakhoze kuwasonyeza iwo, cholembedwa pakhoma. Ife tikudziwa ziripo. Inu mukhoza kuziseleula izo ndi nthabwala, ndi Hollywood, televizioni, kapena kukhala kunyumba ndi kumachinyalanyaza Icho ngati inu mukufuna kutero.

¹¹⁴ Koma mwamuna weniweni wobadwa-kachiwiri kapena mkazi yemwe ali nako kuzindikira kwa Mzimu Woyera apeza malo ake mu mpingo, azipembedza ndi kumawalirira, ndi kumachita zonse zomwe ziri mmoyo wake, kuti ayesere kuwabweretsa mkati ochimwa. Ndithudi. Ngati ali Mulungu, tiyeni. Inu muyenera kuti muike mtima wanu mu izo, ngati inu muli nako kuzindikira. Gwirani ntchito!

¹¹⁵ Musati muzingopita ndi kumati, “Inde, ine ndikuzikhulupirira Izo. Icho ndi Choonadi. Izo ndi zabwino. Ameni,” nkumapita kwanu.

¹¹⁶ Pitani kukagwira ntchito. Inu muli nako kuzindikira. Gwirani ntchito kukadali Kowala, pakuti usiku ukudza pamene palibe munthu angakhoze kugwira ntchito. Gwirani ntchito pamene ife tikadali nacho chitseko chotseguka. Gwirani ntchito pamene ife tikukhoza kumakhala nayo misonkhano yonga iyi. Abweretseni okonedwa athu mkati. Abweretseni iwo ku Uthenga. Tiwatengere okonedwa athu, oyandikana nawo athu. Mulungu anawafera anthu amenewo. Ndipo ife tiyenera kukhala tiri okhudzidwa mokwanira, nawo, kuti tizigwira ntchito mpaka manja athu aziwukha magazi. Ife tidzabwera opanda kanthu ngati ife sititero.

¹¹⁷ Monga msungwana wamng’ono uko ku Kentucky, yemwe wafa posachedwapa uko ku mapiri, kutali ndithu. Uko kunali pafupi ana eyiti. Msungwana mmodzi wamng’ono, pafupi wa cha pakati pa iwo, wa pafupi usinkhu wa zaka thwelofu. Azilongo ake ndi abale, anali aulesi kwambiri, iwo samachita kalikonse. Ndipo amayi awo atagona, akufa ndi matenda owopsya a chifuwachachikulu. Ndipo msungwana wamng’onoyo, iye anali kukolopa, kuphika, kuchapa, kuwasamalira amayi ake, pamene ena onse awo ankalova pomwepo, kumasewera ndi kumapita kukasambira.

¹¹⁸ Potsiriza, amayi akewo anafa, ndiyeno msungwana wamng’onoyo amayenera kuti azipitirizabe chifukwa palibe wa iwo akanamagwira ntchito. Ndipo iye amagwira ntchito nagwira ntchito, ndipo iye ankagwira ntchito mpaka, potsiriza, iye anatenga matenda owopsya, kusowa kwa zakudya, ndi posakhala ndi zokwanira kuti azidya, ndi zina zotero. Thupi la kanthu kakang’onoko linafooka. Iye anali kufa.

119 Mphunzitsi wina wa Sande sukulu anadza kwa iye, anati, “Kodi iwe ndi Mkristu?”

Iye anati, “Inde, nchomwe ndiri.”

Anati, “Kodi ndiwe wa chipembedzo chanji?”

Iye anati, “Ine si wa chipembedzo chirichonse.”

120 Anati, “Ndiye ndiuzeni ine, ukakumana naye chotani Yesu mu dzikoli? Kodi iwe udzamusonyeza chiani Iye, cha mpingo womwe iwe uliko?”

Iye anati, “Iye ndidzangomusonyeza Iye manja anga. Iye adzamvetsa.”

121 Ine ndikuganiza ndi chimene Iye ati adzayang’anepo, tonse ife, pamene ife tikuwona misonkhano yonga umene ukuchitika panowu. Iye adzayang’ana mmanja mwathu ndi kudzawona zomwe ife tachita nawo, kuzindikira kwauzimu.

“Kusalizindikira Thupi la Ambuye.”

Tiyeni ife tipemphere.

122 Ngati manja awo ayenera kuti akhale akugwira ntchito, ndipo inu mukudziwa iwo ayenera kukhala ali, kodi inu simuwatukulira iwo kwa Mulungu ndi kumupempha Iye kuti awayeretse manja awo ku ntchito Yake, pamene ife tikupemphera? Kwezani mmwamba manja anu.

123 Ambuye, tayang’anani pa manja awo. Ndi anga, nawonso, Ambuye. Ine ndikufuna kuti ndibwere ngati msirikali wa zikang’a. Ine sindikufuna kuti ndibwere wopanda kanthu. Ine ndikufuna ndizilalikira mpaka ine ndidzafe. Ine ndikufuna kukoka ndi kupempha, ndi kumasala ndi kupemphera, pakuti ine ndikudziwa mithunzi ya usiku ikugwa ndipo ora likhala posachedwa liri pafupi. Ambuye, tsegulani maso anga, kuti ndiwone zizindikiro zina za Kudza Kwanu. Muiwotche mitima ya anthu awa, usikuuno, ndi zodabwitsa zazikulu zomwe Inu munazilonjeza.

124 Pamene ife tikuwona kuneneratu kwa dziko, ndi kumumva munthu wochimwa kwambiri akufuulira uko, iye “awasesa achikapitolisitiwo.” Ife tikuzindikira kuti iwo ali nawo mabomba uko oti achitire nawo izo; wotentheka wina basi kuti angoligwira ilo. Inu mukuziletsa, mwachifundo, mpaka Inu mutawukonzeketsera Mpingo Wanu.

125 Ambuye, pali chiani pano usikuuno, tikonzeketsereni ife. Ikani mitima yathu mu ntchito. Tisonyezeni ife Kukhalapo Kwanu, pakuti ife tikukhulupirira kuti Inu munauka kwa akufa, ndipo Mzimu wathu ukuzindikira kuti Inu muli pano, Yesu yemweyo, dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Inu muli pano, mu mawonekedwe a Mzimu Woyera, kuti muzigwira ntchito kupyolera mu Mpingo Wanu, kuti muzichiritisa ndi kuti muzipulumutsa. Timveni ife, Ambuye, pamene ine

ndikuwapereka kwa Inu anthu awa ndi mwiniwanga, mu Dzina la Yesu, Mwana wa Mulungu. Amenii.

¹²⁶ O, pofuna chifundo Chake, pofuna ubwino Wake! Ine ndikungomverera kutsukidwa kwenikweni. Izo zinali pa mtima wanga. Ine ndimayenera kuti ndizinene izo. Ine ndikuyembekeza sindinamuvulaze mzanga wa Methodisti, Baptisti, kapena wa Chipentekoste. Ngati ine ndatero, ine sindimalinga kuti ndikuvulazeni inu. Ine ndimafuna kuti ndikuchangamutseni inu, ndikugwedezeni inu pang'ono. Ife tiri pa mapeto.

¹²⁷ “Osakhala nako kuzindikira kwa Thupi la Ambuye; kudzipatula tokha, powoneka kuti tiribe Chikhulupiriro.”

¹²⁸ Ngati inayamba yakhalapo nthawi yomwe tinkafunana aliyense wa inu, ndi pakali pano. Inu mukundisowa ine, ndipo ine ndikukusowani inu. Mulungu akutisowa tonse ife. Tiyeni tilumikizane mitima yathu ndi kuyesetsako palimodzi. Tiyeni tisamaganize, chifukwa ndife a Nazarene, a Pilgrim Holiness, a Katolika, a Presbateria, a Achipentekoste, kapena chomwe ife tiri. Tiyeni tikhale Akhristu. Tiyeni tilizindikire Thupi la Ambuye, ndipo tifikire nkono, mpaka ngakhale kwa wochimwa woyipitsitsa, ndi kuwabweretsa iwo mu khola. Ndilo pemphero langa lodzichepetsa.

¹²⁹ Mngelo wa Mulungu uja Yemwe anabwera ku Sodomu, Iye anabwera. Iye analonjezedwa. Kumbukirani, Mngelo yemweyo anabwera. Aliyense akudziwa kuti Uyo anali Mulungu. Silinali thupi lija, chifukwa thupilo linali fumbi.

¹³⁰ Ine ndinayankhula izo kwa winawake, si kale litali, kuti, “Ujaju anali Mulungu,” ine ndinatero.

¹³¹ Iye anati, mtumikiyo, iye anati, “O, tsopano, M'bale Branham, inu simukukhulupirira kuti Munthu ameneyo anali Mulungu?”

¹³² Ine ndinati, “Iye anali Mulungu. Abrahamu anati Iye anali. Iye anamutcha Iye, ‘Elohim.’ Ameneyo ndi Mulungu Wamphamvuzonse. Iyeyo; ndi Angelo awiri.”

Iye anati, “Chabwino, inu mukuganiza kuti Iye ankakhala mu thupi?”

Ine ndinati, “Izo ndi zophweka kwambiri.”

¹³³ Ndife opangidwa kuchokera mu zipangizo sikisitini; mafuta, kuwala kwadziko, ndi kasiyamu, potashi, zina zotero. Mulungu anangodzisonkhanitsira yekha zodzaza mdzanja pang'ono, nkuti, “Psfyu,” nati, “lowa mmenemo, Gabrielo. Psfyu; lowa mmenemo. Mikaeli.” Ndi kuuzira limodzi la Iyemwini. Anati, “Ine ndamva kuti Sodomu ali pafupi kucha. Tiyeni tipite uko ndi kukawona. Tiyeni tipite uko, eniathu. Abrahamu wakhala akulalikira, ndi enanso akhala akulalikira. Tiyeni tipite tikadziwonere eniathu.”

¹³⁴ Ndipo kodi iwo anabwera kwa ndani? Kwa Osankhidwa. Mmodzi uyu anatsalira mmbuyo, ankayankhula ndi Abrahamu, ndipo Abrahamu anamutcha Iye, “Elohim.” Penyani L wamkulu uyo ndipo muwone ngati uko si kulondola. Ambuye Mulungu Yehova anali mu thupi la mnofu.

¹³⁵ Inu simukuzindikira basi zomwe Mulungu ali. Mulungu akhoza kungoti, “Psfyu.” Ndine wokondwa ine ndikumudziwa Mulungu ameneyo. Limodzi la masiku awa ine sindidzakhala kanthu koma mwinamwake phulusa la chiphala chamoto, koma Iye adzayankhula ndipo ine ndidzabwerera ku moyo kachiwiri. Iye ndi Mulungu.

¹³⁶ Mkazi wanga anati, osati kale litali, anati, “Billy, iwe watsala pang’ono kukhala ndi mutu wa dazi.”

Ine ndinati, “Ine sindinalitaye limodzi lake.”

Iye anati, “Liri kuti ilo?”

¹³⁷ Ine ndinati, “Ndiuze ine kumene ilo linali ine ndisanalipeze ilo; ine ndikuuza iwe kumene ilo likundiyembekezera kuti ine ndibwereko.”

¹³⁸ Ndi kulondola. “Palibe tsitsi limodzi la mmutu mwanu liti lidzatayike.” Mulungu wa Kumwamba, [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Yemwe amalamulira zinthu zonse, adzati, “William Branham,” kapena zina zotero, “bwera apo,” ndipo ine ndidzabwera mu mawonekedwe Ake. Aleluya!

¹³⁹ Mulungu yemweyo, mwa Mzimu Woyera, akukhala pakati pathu, usikuuno, mu ulemerero wa Shekinah, akudzitsimikizira Iyemwini mwa zizindikiro zachirengedwe zomwezo zimene Iye ankachita.

¹⁴⁰ Ngati nthambi ibala mphesa lero, iyo idzabala mphesa mawa. Ngati iyo ndi nthambi ya mphesa, iyo nthawizonse izikhala ndi mphesa. Ife sitidzakhoha konse kulowamo mwa luntha. Ife tidzayenera kudzabwera umo mwa Mzimu Woyera, chifukwa ndiwo mtundu wokha wa Mzimu umene Mpingo wa Mzimu Woyera umabala; zipatso za Mzimu, Moyo wa Khristu mwa ife.

¹⁴¹ Mngelo yemweyo ali pano, mboni Sodomu ndi Gomora asanawonongedwe, kupita ku chiwonongeko.

¹⁴² Tsopano tiyeni tiwone. Ndi angati ali ndi makadi a pemphero? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Alipo forte kapena fifite. Ndi angati omwe alibe makadi a pemphero? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino, alipo kuchulukitsa katatu. Chabwino.

Ine ndikumverera kutsogozedwa kuti ndichite chinachake.

¹⁴³ Tiyeni tingowatenga iwo omwe alibe makadi apemphero. Siyani awo omwe ali ndi makadi apemphero, mwinamwake. . . Chabwino, iwo akhoza kulowamo, nawonso. Koma pa

kuzindikira uku, ife tikufuna iwo okha opanda makadi apemphero. Kwezani manja anu kachiwiri, iwo omwe akudwala ndipo alibe khadi lapemphero, kotero ine ndikhale nalo lingaliro yemwe inu muli. Chabwino.

Pano pali chiwonetsero.

¹⁴⁴ Kodi inu mukukhulupirira ine ndakuuzani inu Choonadi? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mukukhulupirira muli nako kuzindikira kwauzimu, kodziwa kuti Icho ndi Choonadi? [“Ameni.”] Ife sitimasowa kubwera pamwamba pano.

¹⁴⁵ Ine sindine mchiritsi. Ine ndine munthu. Ine ndine m’bale wanu. Khristu ndiye mchiritsi wanu, ngati inu mungakhoze kungomuzindikira Iye kuti ali muno.

¹⁴⁶ Tsopano, ngati zifika pokuchiritsani inu, ngati Iye akanati aime pomwe pano atavala suti iyi, Iye sakanati akuchiritseni inu, chifukwa Iye anachita kale izo. Iye akanakhoza kokha kutsimikizira kuti Iye anali Khristu. Inu mukanadziwa motani izo? Ndi chipatso cha Mzimu, inu mumamudziwa Iye. Kodi Iye anachita moyo wa mtundu wanji?

¹⁴⁷ Kodi Iye anachita chiani pamene Iye anali kuno, kuti atsimikizire kuti Iye anali Mesiya? Pamene iye anasonyzedwa, Petro ndi Yohane, kapena Petro ndi Nataniele, ndi iwo, powauza iwo omwe iwo anali, kumene iwo ankachokera, icho chinali chizindikiro kwa Ayuda. Uko kunali kutsekera kwa m’badwo wawo.

¹⁴⁸ Uko kunali mtundu wina wa anthu akumuyembekezera Iye kuti adze, awo anali Achisamaria, omwe ali theka Myuda ndi theka Wamitundu. Iye anamuza mkazi pa chitsime za machimo ake, ndipo iye anachizindikira icho kuti chinali chizindikiro cha Mesiya. Iye anati, “Ife tikudziwa kuti Mesiya azidzatiuza ife zinthu izi, koma Inu ndinu yani?”

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

¹⁴⁹ Tsopano, Iye sanapite kwa Amitundu (anatero Iye?), pakuti Amitundu sanali kumuyembekezera Iye.

¹⁵⁰ Ndi angati akukhulupirira kuti Mulungu ndi wopandamalire? Ndithudi, Iye ndi wopandamalire. Ndiye Iye sangakhoze kunena chinthu chimodzi kapena kuchita chinthu chimodzi *kuno*, ndi kukachita chinachake cha *uko*, ndi kukhala wolungama. Iye ayenera kumachita chinthu chofanana. Ngati Iye ali nako kachitidwe kabwinoko, ndiye Iye akanati achite izo pa malo oyamba; pamene Mulungu aitanidwa powonekera kwa chirichonse, ndi chiweruzo chimene Iye amapanga apo.

¹⁵¹ Ngati wochimwa mmodzi analirira konse kwa Mulungu, ndipo Mulungu anamupulumutsa iye pa zoyenereza za chikhulupiriro chake, Iye ayenera kuti amupulumutse wochimwa wotsatirayo, ndi wochimwa wotsatira, ndi wochimwa

wotsatira. Iye ayenera kuzichita izo nthawi zofanana, kapena Iye anachita molakwitsa pamene Iye anamupulutsa wochimwa woyamba.

¹⁵² Ayenera kuti azichita chinthu chofanana pa kuchiritsa. Iye anaitsirizitsa kale ntchito iyo. Chinthu chokha, chimene, inu muyenera kuti muchizindikire icho. Iye si nthano. Iye si mulungu wambiriyakale wina. Iye ndi Mulungu, wa pakali pano, “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,” pakali pano. Kodi inu mukukhulupirira Iye ali pano? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mungazindikire izo?

Ine ndikufuna kuti nditembenuzire nsana wanga kwa omvetsera awa. Ine ndipemphera.

¹⁵³ Mzimu Woyera utsimikizira zomwe ine ndanena usikuuno, pa kutseka kwa Uthenga uwu, kuti zizindikiro zofanana zimene Yesu anati zinaperekedwa kwa Sodomu zidzaperekedwa kwa kam’badwo kano. “Monga izo zinali mu masiku a Sodomu, chomwecho izo zidzakhala ziri mu Kudza kwa Mwana wa munthu.” Ndiye inu muuzindikire Mzimu umene uli pano.

¹⁵⁴ Anali ndani uja, kachiwiri, amene akudwala ndipo alibe khadi lapemphero? Ife tikufuna tiwatenge makadi apemphero. Ife tikuti tiwapempherera iwo onse.

¹⁵⁵ Tsopano, ine sindingakhoze kukuuzani inu kuti uyu ndi ndani. Mulungu akudziwa. Poyamba, ine ndikungofuna kuti ndimupeze winawake yemwe Mzimu Woyera... Aliyense wa inu, tsopano ingoyambani kupemphera ndi kumati, “Ambuye, khalani achifundo tsopano kwa ine ndi kundithandiza ine.” Ndipo muwone ngati Iye angachite monga Iye anati Iye akanati azidzachitira.

Ine ndikungoyang’anira chizindikiro Chake.

¹⁵⁶ Ndi angati akudziwa kuti Yesu, lero, ali Lawi la Moto lomwe linkawatsatira ana a Israeli? “Ine ndinachokera kwa Mulungu, ndipo ndikupita kwa Mulungu.” Kodi izo ndi zomwe Iye ananena? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo pamene Paulo anakomana naye Iye pa njira yopita ku Damasiko, kodi Iye anali chiani? Kuwala kwakukulu, Lawi la Moto. Iye ali Mmodzi yemweyo lero, Mzimu Woyera wa Mulungu. Thupi la Yesu liri ku dzanja lamanja la Mulungu, pa Mpandowachifumu Wake Kumwamba; koma Mzimu Wake uli pano pa dziko lapansi, kutsirizitsa ndi kuthetsa ntchito Yake.

¹⁵⁷ Ndipo Mzimu womwewo umene unkakhala mu thupi la Yesu Khristu, unali Mzimu womwewo umene unali mwa Mngelo uja yemwe anadza ku Sodomu ndi Gomora. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Yemwe uja amene ankawatsatira ana a Israeli; Mulungu yemweyo.

158 Yesu anati, “Ine ndine Thanthwe lija lomwe linali mu chipululu. Makolo anu ankadya manna, ndipo iwo anafa. Ine ndine Mkate wa Moyo umene unachokera kwa Mulungu, kuchokera Kumwamba. Ine ndine Mkate umenewo. Ine ndine Thanthwe limenelo.”

159 “Bwanji, Iwe ukuti Iwe unamuwona Abrahamu, ndipo Iwe sunapitirire usinkhu wa zaka fifite.”

160 Iye anati, “Abrahamu asanakhalepo, INE NDINE.” Kodi INE NDINE anali ndani? Kuwala koyaka kuja kumene kunali mu chitsamba, kumene kunayankhula kwa Mose.

161 Iye ali Yesu yemweyo usikuuno. Ndilo neno. Si choncho? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ine ndikutsutsa nazo, ndikutsutsa wokhulupirira aliyense kuti akhulupirire izo.

162 Dona wamng’ono uyu wakhala apa, kanthu kakang’ono koyera pa chipewa chake. Inu muli ndi khadi lapemphero? Inu mukudwala? Kodi ndife alendo kwa wina ndi mzake? Mulungu akutidziwa ife tonse. Pali Kuwala pa mkaziyo, ngati inu mungakhoze kukuwona Iko kukuzungulira pamwamba pa iye. Iye anali kupemphera. Ndi kulondola uko? Ayi, inu mulibe mwayi woti mubwere pano, koma inu munali kupemphera. Chifukwa, ine ndikuwona. Pansi chabe pa izo pali mthunzi wakuda. Ndi imfa. Mkaziyo ali ndi mthunzi waku imfa. Iye ali ndi khansara. Kodi inu mukukhulupirira Mulungu akhoza kukuchizani inu? Khansara ya pabere. Ndipo ine ndikumuwona dokotala akuyang’ana pa ilo, ndi iye akukuuzani inu kuti iye ayesa kuti aling’ambe. Ndipo inu mwakonzekera kukang’ambidwa. Ndipo ine ndikukuwonani inu mukuyenda kuchokera pa nsanja, kapena chinachake chimzake. Inu ndinu mlaliki, mlaliki wachikazi. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndi kulondola uko, dona? Chimene Iye ananena, kodi kunali kulondola uko? Imirirani pa mapazi anu ngati uko kuli kulondola.

163 Tsopano kodi inu mukukhulupirira? Kuzi-...Kodi inu mungakhoze kuzindikira kuti ndi Yesu yemwe uja yemwe anakhudza. . . Mkaziyo anakhudza chovala Chake, osati ine; Iye. Ine sindikumudziwa mkaziyo. Iye sakundidziwa ine. Mulungu akutidziwa ife tonse. Mulungu akudalitseni inu, mlongo.

164 Ine ndikumuwona dona mu masomphenya. Iye akupemphera. Iye ndi msungwana, wakhala pomwe *apa*. Pali chinachake chokhudza mwana. Ndi, iye akufuna. . .Ayi, iye anali ndi mwana. Ayi, ndi kupita pachabe. Ndi chimene icho chinali, khanda lakufa. Iye ndi wochokera ku Kentucky. Dzina lake ndi Martin. Inu muli pati, Akazi a Martin? Eya, muli ndi diresi yachikasu. Izo ndi zoono. Si choncho, dona? Imirirani pa mapazi anu ngati ziri chomwecho. Ine sindikumudziwa mkaziyo. Koma Mulungu akumudziwa iye, ndipo ndi uyo apo. Lidalitsike Dzina la Ambuye Mulungu.

165 Kumbuyo komwe kwa iye kwakhala dona. Iye ali ndi zotupa. Iye ali ndi vuto kudzanja lake lamanja, wokhala ngati mkazi wojinja wavala diresi lowoneka mwakuda. Inu muli ndi khadi la pemphero, dona? Inu mulibe? Inu simukulisowa ilo. Kodi inu mukukhulupirira kuti inu munali nacho chikhulupiriro kuti mukhudze Chinachake? Inu simunandikhudze konse ine. Inu munamukhudza Iye. Chabwino. Ndiye kwezani mmwamba dzanja lanu liri ndi mpango mmenemolo, ndi kulandira machiritso anu. Pitani kwanu ndipo mukachire, mu Dzina la Yesu Khristu.

166 Yang'anani kuno. Apo pakhala dona wamng'ono kumbuyo kuno wavala diresi ya mandalasi. Iye waweramitsa mutu wake. Iye akuwapempherera abambo ake. Iwo ali ndi vuto la impyso. Inu mukukhulupirira Ambuye awachiza iwo, mlongo? Inu mukukhulupirira izo? Ndiye inu mukhoza kukhala nazo izo.

167 Dona, inu munali wachifundo kwambiri kwa iye, kuti munamuza iye kuti anali iyeyo. Chifukwa chimene inu munanenera izo, chifukwa Mzimu Woyera unasunthira kumene pa inu, aponso. Ndiko kulondola. Inu muli ndi khadi lapemphero? Inu mulibe? Inu simukulisowa ilo. Inu mukuwapempherera amanu. [Mlongoyo ati, "Inde."—Mkonzi.] Ndipo inu mukuganiza zowabweretsa iwo ku tchalitchi mawa usiku. ["Inde."] Ndiko kulondola. Simukusowa kuti muchite izo. Mukaike manja anu pa iye ndi kukaitanira pa Dzina la Ambuye Yesu. Iye akakhala bwino, ngati inu muti mukhulupirire izo.

168 Ine ndikutsutsa chikhulupiriro chanu. Ndi ndaninso yemwe alibe khadi la pemphero ndipo akufuna kuti akhulupirire?

169 Inu, mwakhala apa patsogolo, inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu? Mneneri ndi mtumiki waku m'badwo. Kodi inu mukukhulupirira kuti ine ndiri nawo Uthenga wa Mulungu? [M'bale ati, "Inde."—Mkonzi.] Inu mukutero? Ine sindikukudziwani inu. Koma Mulungu akukudziwani inu. Ngati Mulungu angandiuze ine mavuto anu, kodi inu muzilandira izo ngati machiritso anu, mukhulupirira kuti ndi Ake? Inu mukhoza kuzindikira ndiye, izo? Ngati mzimu wanu ungakhoze kumugwira Iye tsopano pamene ine ndikuyankhulana kwa inu, ndiye inu mulandira machiritso anu. Mutero inu? Ndi pachifuwa panu, minofu yovulazidwa. Ndipo pambali pa izo, ndinu mlaliki. Ndiko kulondola. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukhulupirireni Mulungu.

Nditembenuza nsana wanga.

170 Zipempherani, onani ngati Iye ali Mngelo yemweyo, muwone ngati ali Mulungu yemweyo yemwe analonjeza, pamene Iye anali ndi nsana Wake utatembenezidwira ku hema. Zipempherani, ena a inu, kuti Ambuye Mulungu, Yemwe anatuma Mngelo Wake, ndi kudzatsimikizira kuti Sodomo anali ku...Mapeto anali pafupi.

171 O Ambuye Mulungu, mutumizeni Mngelo Wanu, usikuuno, ndipo mupereke kuzindikira komweko, chifukwa ndi lonjezo la Mwana Wanu. Ndipo mulole izo zikhale chomwecho.

172 Mkazi waima patsogolo pa ine, ndipo iye akuvutika ndi liwombo pa mutu. Iye ali mmbuyo kumbali *iyi*, pakuti ine ndikumverera iye akukoka, chikhulupiriro chake. Dzina lake ndi Abiti Wiley.

173 Kodi iye ali kuti? Tiyeni tiwone. Mmbuyo *umu* penapake. Chirichonse chimene dona. . . Apo, kodi zinali zoonza izo, dona? Chabwino. Pitani kunyumba ndipo mukachiritsidwa.

Khalani nacho chikhulupiriro mwa Mulungu. Ena nonse inu zipempherani, penapake.

Mulole izo zidziwike, O Ambuye, Inu ndinu Mulungu.

174 Pali mkazi waima patsogolo panga, yemwe akupemphera kumbuyo mwa omvetsera, ndipo iye ali ndi zosokonezeka. Iye wavala diresi la mandalasi ofiira ndi oyera. Dzina lake ndi Akazi a Lake.

175 Muli pati inu, Akazi a Lake? Imirirani pa mapazi anu, paliponse. Mulungu akudalitseni inu. Pitani kwanu ndipo mukachiritsidwe. Chikhulupiriro chanu chakupulumutsani inu.

176 Ndi Yesu yemweyo. Ndi Mngelo yemweyo. Kodi inu muli nako kuzindikira? Lizindikireni Thupi la Ambuye. Kodi inu mukukhulupirira kuti ine ndikukuuzani inu Choonadi? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mukukhulupirira kuti Khristu akupereka umboni wa izo? [“Ameni.”] Ngati inu mukukhulupirira izo, kwezani mmwamba manja anu.

177 Ndi okhulupirira angati ali muno, angagwedeze manja awo monga *chonchi*? Ndiye, inu mundikhulupirire ine, monga mneneri wa Mulungu. Musati mukaikire, kamodzi mochepa. Atengeni manja awo omwe inu mukuwagwedezera kwa Mulungu, ndipo muwaike pa winawake pafupi ndi inu, ndipo inu muwona ulemerero wa Mulungu. Ndizo zonse zomwe Iye angakhoze kuzichita. Kodi inu mungakhoze kulizindikira Thupi la Ambuye? “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira: ngati iwo aika manja awo pa odwala, iwo adzachira.”

178 Ambuye Mulungu, Mlengi wa kumwamba ndi dziko lapansi, Mwini wa Moyo wosatha, mpangeni Satana amasule wokhulupirira aliyense mkati muno. Iwo aikana manja pa wina ndi mzake, ndipo iwo ndi okhulupirira. Iwo ali nacho chikhulupiriro mwa Mulungu, ndipo iwo akukhulupirira kuti Inu muzichita izo. O Ambuye, Mawu Anu sangakhoze kulephera, osati ngakhale malonjezo Anu. Ndipo malonjezo Anu anali, “Ngati iwo aika manja awo pa odwala, iwo adzachira.”

179 Tsopano, Satana, iwe chiwanda choipa chopsynja, yemwe wawamenyera anthu awa pansu ku fumbi, ine ndikukulamulira

iwe mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo, kuti iwe uwamasule iwo. Tuluka mwa iwo, mu Dzina la Yesu Khristu.

¹⁸⁰ Tsopano muyike manja anu pa wina ndi mzake, ndipo mupemphere pemphero la chikhulupiriro. Ndipo pamene inu mukumverera Mzimu wa Mulungu, muuzindikire Iwo, kuti ilo ndi lonjezo la Mulungu kwa inu.

¹⁸¹ Aliyense yemwe angakhoze kumverera kuti mphamvu ya Mulungu ikuyenderera mwa inu, imani pa mapazi anu ndipo mulandire machiritso anu. Ine ndikukulamulirani inu, mu Dzina la Yesu Khristu, aliyense wa inu okhulupirira, kuti muime pa mapazi anu ndipo mumulandire Yesu ngati mchiritso wanuwanu. Dzukanimo, inu mu zikuku izo, mmachira, chirichonse chomwe chiri. Dzukanimo. Mukhulupirireni Mulungu. Mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, chiritsidwani.

¹⁸² Iwo akuwuka, kuchokera mmachira ndi mzikuku, ndi chirichonse.

Chabwino, M'bale Sullivan.



KULIZINDIKIRA THUPI LA AMBUYE CHA59-0812
(Discerning The Body Of The Lord)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham woperekedwa mu Chingerezi Lachitatu usiku, Ogasiti 12, 1959, ku Miami Valley Chatauqua Campgrounds mu Chatauqua, Ohio, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa m'chaka cha 2002 ndi Voice of God Recordings:

CHICHEWA

©2002 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org